# CHIKALAKALA CHA NEHEMIAH.

ABRIDGED VERSION OF THE BOOK OF NEHEMIAH IN THE NYANJA LANGUAGE, CENTRAL AFRICA.

*(TENTATIVE EDITION.)*

LONDON:
CHALEMBEDWA PA
BRITISH AND FOREIGN BIBLE SOCIETY.
1894.

# CHIKALAKALA CHA NEHEMIAH.

## CHAPTER I.

1 Mau ya Nehemiah mwana wa Hakaliah.
Idalipo mwezi wa Chisleu, chaka cha makumi
awili, apo nidali pa Shushan, chinyumba,
2 Kuti Hanani, mmoji wa abale wanga,
anaja, iye ni wena kuchokera pa Yudeya; ndipo
nidawafuncha awa nkani za WaYehudi awo
wadapulumuka, ni nkani za Yerusalem.
3 Ndipo wadanifotokozela kuti awo wachela
awo wosiidwa wa mikole paja pa jiko wali pa
kusauchidwa kwakukulu ni kukoja: pupa ncho
ya Yerusalem yagumulika, ni vicheko vake
vabuchidwa moto.
4 Idalipo apo nidava mau aya, nidakala
panchi kulila misosi, ni kuchita malilo masiku
ena ena; ndipo nidamanga vakudya ni kupempa
pachogolo pa Mulungu wa pamwamba
5 Ni kunena, Ndikupembeza, Yahveh Mu-
lungu wa pamwamba, wakusunga chilanga ni
lisungu ni awo wakumkonda ni kusunga ivo
anavilangiza:
6 Makutu yako yasongoke, ni maso yako
yachekulidwe kuti uveche pempero la kaporo
wako, ilo nipempa pachogolo pako masiku ano
usana ni usiku, kwa wana wa Israel akaporo
wako, apa nivomera thambi za wana wa Israel:
izi tinazichita kukulakwila: etu, ni ine ni
chilawa changa tachita thambi.
7 Takuchitila voipa nditu, wosasunga ivo
unatitaukila ni vija unatiikila ni vija unatila-
mulila ivo udamgwiriza kapolo wako Musa.